Muziona Moyo Ngati Mmene Mulungu Amauonera (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 13.
Bukuli likupezekanso pa www.jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



N'CHIFUKWA CHIYANI MULUNGU AMALETSA KUGWIRITSA NTCHITO MAGAZI MWACHISAWAWA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena akhoza kunena zotani pa nkhaniyi?

_____

_____

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

_____

_____

Chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Mulungu amaona kuti magazi ndi opatulika

(Werengani mutu 13 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 10-16.)

Werengani Genesis 9:3, 4; Levitiko 17:13, 14.

N'chifukwa chiyani Mulungu amatiletsa kudya magazi?

Werengani Machitidwe 15:28, 29.

Kodi Mkhristu ayenera kumwa magazi kapena kudya nyama yomwe siinakhetsedwe magazi? Nanga kodi ayenera kuikidwa magazi?



Ngati adokotala atakuuzani kuti musiye mowa, kodi mukhoza kumangodziika dilipi ya mowawo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Chilamulo cha Mose chinafotokoza njira imodzi yokha yoyenera kugwiritsa ntchito magazi.

(Werengani mutu 13 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 17-19.)

Werengani Levitiko 17:11.

Kodi kugwiritsa ntchito magazi popereka nsembe kunkathandiza bwanji anthu a Mulungu kalelo?

Werengani Yohane 3:16; Aheberi 9:11, 12.

Kodi Yesu anakwaniritsa chiyani polola kupereka moyo wake ngati nsembe?

Kodi mumamva bwanji mukaganizira kuti Yesu anapereka moyo wake chifukwa cha inuyo?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI…

Zimene Baibulo limanena zokhudza magazi ndi zachikale.

MUNGAYANKHE KUTI…

Ndi zoonadi kuti zimene Baibulo limanena pa nkhani ya magazi zinalembedwa kalekale. Koma ndimakhulupirira kuti mfundo zake zimagwirabe ntchito kwa Akhristu masiku ano chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

NGATI WINA WANENA KUTI…

Bwanji ngati adokotala atanena kuti umwalira ngati suikidwa magazi?

MUNGAYANKHE KUTI…

Ngati zinthu zitafika poipa kwambiri, kodi pali aliyense amene anganene motsimikiza kuti *sindifa* ngati nditaikidwa magazi? Koma pali winawake amene amatitsimikizira kuti adzatipatsanso moyo ngati titafa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania